



MUTU 2:

ABRAHAMU

PANALI MUNTHU WINA
WOTCHEDWA ABRAHAMU AMENE
ANKAKHULUPIRIRA KUTI
MAFANO NDI SI MILINGU.



ANKADZIWA KUTI MULLINGU
NDI MLENGI NDIPO KUTI
SAYENERA KUPEMBEDZEDWA
KUPYOLERA M'MAFANO.

MULLINGU ADAMUZA KUTI,
"ABRAHAMU, USIYE MZINDA
WAMAFANOWU. SIYA ABALE AKO
NDI DZIKO LAKO NDIPO
NDIDZAKUWONETSA KUMENE
UYENERA KUPITA. NDIDZACHITITSA
KUTI UKHALE TATE WA MTUNDU
WAKULU. NDIDZADALITSA ONSE
AMENE ADZAKUDALITSA NDIPO
NDIDZATEMBERERA ONSE AMENE
ADZAKUTEMBERERA. NDIPO
KUPYOLERA MWA IWE MITUNDU
YONSE YA PA DZIKO LAPANSI
IDZADALITSIKA."



KODI ABRAHAMU NDIYE
MWANA WOLONJEZEDWA
AMENE ADZAPHWANYA
TCHIMO NDI IMFA?

PAFUPIFUPI 1921 B.C.



ABRAHAMU ADADZIWA KUTI
MAU AMENE ADAAMVA ANALI
MAU A MULLINGU, CHONCHO
ANAMVERA, NGAKHALE KUTI
SANKADZIWA KUMENE ADZAPITE
TSOPANO. ANKADZIWA
KUTI WASIYA MAFANO M'MBUYO
NDIPO KUTI AKUTSATA
MULLINGU WAMOYO. ZIMENEZI
ZINAMKWANIRA ABRAHAMU.
KOMA PA ULENDOWO
ANATENGA LOTI MPHWAKE.

ABRAHAMU ANAYENDA MPAKA
ANAFIKA M'DZIKO LA
KANANI. KUMENEKO MULUNGU
ANAYANKHULA NAYE:

**ABRAHAMU ULIYENDERE
DZIKOLI MBALI ZAKE ZONSE.
NDIDZAPEREKA DZIKO LA KANANILI
KWA ANA AKO AM'TSOGOLOMO.
NDIDZACHITITSA KUTI UKHALE NDI
ANA AMBIRI, OSAWERENGEKA.
ADZACHULLUKA NGATI MCHENGA
WA PA DZIKO LAPANSI.**





SARA, MULLINGU WANDIENZA
KUTI UDZAKHALA NDI ANA NGAKHALE
KUTI ZAKA ZAM'MBUYO ZONSEZI
SUNABEREKEPO.

MULLINGU
ANATI
UDZABEREKA.

UKUDZIWA KUTI
SINDINABEREKEPO
MWANA, NDIPO PANO
NDAFIKA MSINKHU WOTI
SINDNGABEREKENSO.
NDINGABEREKE
BWANJI?

GENESIS 12:1-3, 13:14-17

ABRAHAMU AMATI
AKAYENDAYENDA
M'DZIKOLO, ANKAIMA
NTHAWI ZINA NDI
KUPEREKA NSEMBE
YAMAGAZI. MONGA
ABELE, ABRAHAMU
ANKAPEREKA NSEMBE
MWA CHIKHULLUPIRIRO.



NSEMBE YAMWANAWANKHOSA INKALEPHERA NDITHU
KUCHOTSA MACHIMO AKE. KOMA PAMENE MULINGU
ANAWONA CHIKHULLUPIRIRO CHA ABRAHAMU, MULINGUYO
ANAKWIRIRA TCHIMO LA ABRAHAMUYO.



PATAPITA ZAKA KHUMI

ABRAHAMU, ZAKA
KHUMI ZAPITAZI UNATI
MULUNGU ADAKUUZA KUTI
NDIDZABEREKA MWANA.
TSOPANOTU NDINE WA ZAKA 75
NDIPO IWE NDIWE WA ZAKA 85.
TILIKUKALAMBA, KOMABE TILIBE
MWANA. POSACHEDWAPA
UDZAKALAMBA KWAMBIRI KOTERO
KUTI SUDZATHA KUBEREKA. KODI
NZOONA KUTI MULUNGU
ADAKUUZADI ZIMENEZI?



NDIKUDZIWA KUTI NDI
MULUNGU AMENE ADAYANKHULA NANE,
KOMA SINDIDZIWA CHIFUKWA CHIMENE IYEYO
ADAKAYEMBEKEZERABE. ANANENA KUTI INEYO
NDIDZAKHALA TATE WA MTUNDU WAUKULU ZEDI,
KOMA CHIMENE NDILI NACHO NDI THUPI LANGA
LOKALAMBALI, MKAZI WOKALAMBA WOTI
SANGATHE KUBEREKA, NDI GULU
LALIKULU LA NKHOSA.



**USAOPE ABRAHAMU,
INE NDINE CHITETEZO
CHAKO NDI CHOLOWA
CHAKO CHACHIKULLU.**

**KODI
MUDZANDIPATSA
CHOLOWA CHANJI,
INETU NDILIBE
MWANA?**

**IWEYO
NDI SARA
MUDZAKHALA
NDI MWANA**



**BWERA KUNO
ABRAHAMU, YANG'ANA
NYENEYEZI NDIPO UWONE
NGATI UKHOZA
KUZIWERENGA. MONGA
NYENEYEZI, ANA AKONSO
ADZAKHALA AMBIRI,
OSAWERENGEKA.**

**NDIKUKHULUPIRIRA
KUTI ZIDZACHITIKA MONGA
MWANENERAMU.**

**CHIFUKWA CHA CHIKHULLUPIRIRO CHAKOCHO.
UDZIWE KUTI ANA AKO ADZAKHALA ALENDO M'DZIKO
LOSAKHALA LAO. AKADZAZUNZIKA MONGA AKAPOLO
KWA ZAKA 400, NDIDZALANGA DZIKOLO NDIPO ANA
AKO ADZATULIKA M'DZIKO LIMENELO NDI CHUMA
CHAMBIRI. PAMBUYO PAKE ADZABWERERA KUNO
NADZAKHALA M'DZIKOLI.**



KODI
LONJEZO LA
MWANA LILI
KUTI? TSIKU
NDI TSIKU
NDIKUONJEZERA
KUKALAMBA.
POSACHEDWAPA
SUDZAKHALA
NDI MPHAMVU
ZOBEREKERA.
ABRAHAMU,
SINDIDZATHA
KUKUBEREKERA
ANA.

MWAMBO WA
KUNO NDI WAKUTI
MTSIKANA WANGA WA
NTCHITO AKHOZA
KUNDIBEREKERA
MWANA.



ABRAHAMU, SUKUWONA
KUTI MWAI WATHU WOMALIZA
KUTI TIKHALE NDI ANA NDI
UMENEWU? USACHEDWE
UMTENGE MTSIKANAYU NDIPO
UBEREKE NAYE MWANA.
MWANAYO ADZAKHALA MBEU
YAKO. CHIMENECHI NDI
CHIFUNIRO CHA MULLUNGU.
NANGA PALI NJIRA INANSO
MMENE IWE UNGAKHALIRE
TATE WA MTUNDU
WAUKULU?





NDI NJIRA
YOKHAYI BASI

ABRAHAMU SADAPEMPHERE KWA
MULUNGU. ANAIWALA LONJEZO
LA MULUNGU NDIPO ADAAMVERA
MAU A MKAZI WAKE.

GENESIS 16:1-4


PATAPITA
MIYEZI
YAMBIRI

NDIDZABEREKA
MWANA
WA ABRAHAMU.



PAMENE HAGARA ADADZIWA KUTI
ANKAYEMBEKEZERA MWANA WA
ABRAHAMU ANAYAMBA KUNYADA
NKUMAPEPUTSA SARA. SARA
SANKAKONDWA NDIPO ANAYAMBA
KUCHITIRA NSANJE HAGARA.


SARA ANKAGWIRITSA HAGARA NTC
NDIPO ANKAMUZUNZA. MULLINGU SAN
AKHALE NDI AKAZI AWIRI KAPENANSO
KUPYOLERA MWA MKAZI WOSA



UKAMALIZA
KUTUNGA
MADZI, UWAZE
NKHUNI.

HAGARA ANATHAWA
SARA NDIPO ANAPITA
KU CHIPULULU.


HAGARA ANATHAWA SARA NDIPO A
CHIPULULU. ATATOPA KUTI SAKANATH
ANAKOMOKA. MULLINGU ADAWONA MI
ANKAVUTIKIRA NDIPO ADALANKHI



**HAGARA, BWERERA
KWA SARA NDIPO
UKAMGONJERE.
UDZAKHALA NDI MWANA
NDIPO UDZAMUTCHA
DZINA LAKE ISIMAELE,
KUTANTHAUZA
KUTI 'MULLINGU
AMAMVA.'**



**KUCHOKERA MWA
IYE MUDZATULUKA ANA
AMBIRI, OSAWERENGEKA.
ISIMAELE ADZAKHALA MUNTHU
WA KU TCHIRE. NTHAWI ZONSE
AZIDZAMENYANA NDI
ALIYENSE NDIPO ALIYENSE
AZIDZAMENYANA NAYE.
AZIDZAKHALA PAFUPI NDI
ABALE AKE NTHAWI ZONSE.**



HAGARA ANABWERERA
NDIPO POSAKHALITSA
MWANA ANABADWA.

MULUNGU
ANANDIUZA KUTI, POPEZA
MWANAYU NDI WA ABRAHAMU,
ADZAKHALA TATE WA
MAFLUKO AMBIRI.

ISIMAELE ANAKHALA TATE
WA MAFLUKO A AARABU.

GENESIS 16:4-16


ISIMAELE ANABADWA
PAMENE ABRAHAMU ANALI
NDI ZAKA 86. ATABADWA
ISIMAELE, POSAKHALITSA,
ABRAHAMU ANAKALAMBA
KWAMBIRI NDIPO ZINALI
ZOKAIKITSA KUTI
NKUBEREKANSO. KODI
ISIMAELE NDIYE MWANA
AMENE MULLINGU
ANALONJEZA ABRAHAMU?
KOMA MULLINGU ANATI
MWANA WALONJEZOYO
ADZABADWA KUPYOLERA
MWA SARA NDI ABRAHAMU.





KODI MULUNGU ADZAKWANIRITSA
BWANJI LONJEZO LAKE POPEZA SARA
NDI ABRAHAMU NGOKALAMBA KWAMBIRI,
OSAYEMBEKEZEKA KUBALA ANA.

PAMENE ISIMAELE ANALI NDI ZAKA 13,
ABRAHAMU ALI NDI ZAKA 99, MULUNGU
ANAYANKHULA NAYENSO ABRAHAMUYO.



**ABRAHAMU, INE NDINE MULUNGU
WAMPHAMVUZONSE. CHITA ZONSE
ZIMENE NDIKUKUZA NDIPO USACHIMWE.
MONGA NDINAKUZZAKALENDIDZACHULUKITSA
ANA AKO, NDIPO IWEYO UDZAKHALA TATE WA
MAFUKO AMBIRI. //NDIDZAKHAZIKITSA
PANGANO LANGA NDI IWE KOMANSO NDI
ANA AKO A PAMBLIYO PAKO.**

**NDIDZAPEREKA DZIKO LA
KANANI NGATI CHOLOWA
KWA ANA AKO MPAKA
MUYAYA. SARA
ADZAKHALAWOYEMBEKEZE
RA NDIPO ADZABALA
MWANA MONGA
NDINALONJEZERA,
MWANAYO NDIYE
ADZAKHALE MTSOGOLERI
WA MAFUKO AMBIRI.**



**HA-HA. ZIMENEZI
ZINGATHEKE BWANJI? INE PANO
NDILI NDI ZAKA 99, NDIPO SARA
ALI NDI ZAKA 89. THUPI LANGA LILI
NGATI LA MUNTHU WAKUFA.
SITINGABEREKE. CHONDE MULOLE
KUTI ISIMAELE AKHALE
MWANA WALONJEZO.**

AI, MONGA NDIDANENERA
PACHIYAMBI PAJA, IWE NDI
SARA MUDZAKHALA NDI MWANA
WANUWANU, WOTULUKA M'THUPI
LANU. LONJEZO LA MADALITSO
LIDZAPITIRIRA KUPYOLERA MWA
IYE, OSATI ISIMAELE. CHAKA
CHINA SARA ADZABEREKA
MWANA WAMWAMLINA.




NZOTHEKA?..... INDE. MULLINGU
AMENE ANALENGA THUPI LA MUNTHU,
AKHOZA KUTENGA MATUPI AWIRI
OKALAMBA, MATUPI ONGA A
ANTHUAKUFA, NDI KUWAPATSANSO
MPHAMVU ZOBEREKERA.....ZONADI.
MULLINGU AKHOZA KUCHITA
CHINTHUCHOTERE!





PATAPITA MASIKU ANGAPO, ANTHU
ATATU OCHOKERA M'CHIPULULU
ANAMUWONEKERA ABRAHAMU.
SANKAWONEKA NGATI AYENDA
MTUNDA WAUTALI, KOMANSO
SANALI ANTHU OCHOKERA M'MIDZI
YOYANDIKANA NDI ABRAHAMU.
ANALI AMPHAMVU, ODALIRIKA, NDI
ACHIKHALIRE.

ABRAHAMU ADAWAYANG'ANITSITSA
AKUYANDIKIRA NDIPO ANADZIWA
KUTI ANALI ANTHU OSIYANA NDI
ANTHU ENA, KOMA SANKADZIWA
KUTI ALENDO AKEWO SANALI
OCHOKERA M'DZIKO LINO LAPANSI.




AWIRI A IWO ANALI
ANGELO OLUNGAMA, KOMA
WACHITATUYO ANALI
MULLINGU AMENE
ANKAWONEKANSO NGATI
MNGELO NKUMAYANKHULA
NDI ABRAHAMU. ABRAHAMU
ANAPITA KUKAWALONJERA.



ABRAHAMU,
MKAZI WAKO
ADZAKHALA
NDI MWANA
WAMWAMUNA.

HE-HE-HE

KUKALAMBA KONSEKU!
NDIPO ABRAHANGOKALAMBA
KUPOSA INE, KODI NKUKHALA
NACHOBE CHILAKCHOKHALIRA
PAMODZI MONGA KALE?



NCHIFUKWA CHIYANI SARA
AKUSEKA PAMENE MULLUNGU
AKUTI ADZAKHALA NDI
MWANA?


SINDINASEKE.

UNASEKA.
SUNAKHULUPIRIRE. KODI
PALI CHOSATHEKA NDI MULLUNGU?
NDIDZABWERANSO PAMENE NTHAWI
YOTI UTENGE PATHUPI YAKWANA
NDIPO UDZAKHALA NDI MWANA.



KODI NDIMUZE
ABRAHAMU ZIMENE NDITI
NDICHITE? IYEU ADZAKHALA
TATE WA ANA AMBIRI, NDIPO
ADZAPHUNZITSA ANA AKE
NDI ZIDZUKULU ZAKE
KUNDIMVERA.

INDE
AYENERA
KUDZIWA.



TCHIMO
LA SODOMU NDI
GOMORA LAFIKA POIKA
KWAMBIRI. NDIDZAONONGA
ANTHU ONSE M'MIZINDA
IMENEYI - AMUNA,
AKAZI, NDI ANA.


KOMA MPHWANGA
LOTI NDI BANJA LAKE
AMAKHALA KUMENEKO!

GENESIS 18:10-22



NDIKAKAPEZA
ANTHU OLUNGAMA
50 SINDIKAONONGA
MZINDAWO.

SIKHALIDWE LA
MULLINGU KUONONGA
ABWINO NDI OIPA
OMWE. NANGA MUTAKHALA KUTI
MULI ANTHU OLUNGAM 50
MUMZINDAMO, KODI SIMUD-
ZANONGA MZINDAWCHIFUKWA
CHA ANTHU OLUNGAMA 50?
NDIKUDZIWA KUTI
MUWERUZI WA ANTHU
ONSE ADZACHITA
CHOYENERA.



INE NDINE WOIPA,
WOSAYENERA KUYANKHULA NDI
MULLUNGU, KOMA NANGA ATAPEZEKA 45,
KODI MUDZAWONONGA ONSE CHIFUKWA
CHOPEREWERAPO ANTHU ASANU?

NGATI ATAPEZEKA 45
SINDIDZAWUWONONGA.

SINDIDZAWUWONONGA
NGATI KULI OLUNGAMA 40.

NANGA NGATI
APEZEKAKO 40
OKHA?




MUSANDIPSERE
MTIMA. NANGA
NGATI KULI ANTHU
OLUNGAMA 30?

SINDIDZAWUWONONGA
CHIFUKWA CHA ANTHU
OLUNGAMA 30?

SINDIDZAWUWONONGA
MZINDA WONYANSAWO
NGATI MULI ANTHU
OLUNGAMA MAKUMI
AWIRI M'MENEMO.

NANGA NGATI
KULI MAKUMI
AWIRI?




CHONDE MUSAKWIYE. NDIFUNSA KOMALIZA
TSOPANO. NANGA NGATI MULI ANTHU OLUNGAMA
KHUMI OKHA M'MIZINDAYO, KODI
MUDZAWONONGABE?

AI, NDITAKAPEZA
ANTHU OLUNGAMA KHUMI
SINDIDZAWONONGA
MZINDAWO.



NGATI
SIMUNGAKAPEZE
KHUMI KODI MUNGA
KUKACHENJEZAKO
MPHWANGA LOTI?


TIKAMUYENDERA
USIKU UNO.



ANGELO AWIRI ANAPITA MU
MZINDA MADZULO A TSIKU
LIMENELO NDIPO ANKAYENDA
PAFUPI NDI NYUMBA YA LOTI.


KUNYANSA
KWAKE KWAPOSA MMENE
NDINKAGANIZIRA.

NDAWONA TSOPANO
CHIFUKWA CADZAONONGERE
ALIYENSE, ANA NDI NYAMA
ZOMWE.



EEE, ALENDO
INU, SIMUNGAKHALE MU
MSEU USIKU WONSE, KUMENEKO
NKUIKA MOYO PACHISWE.
TIYENI MUKAGONE KUNYUMBA
KWANGA USIKU UNO.


EEE! NDI
OKONGOLA.
TIKADZIWITSA ANTHU
ENA ZA IWOWA.



LOTI, TITULUTSIRE
ANTHUWO KUTI
TIGONE NAWO.

CHOKANI;
SIMUNGACHITE
CHINTHU CHONYANSA
CHOTERE

AKUDZIYESA
NDANI, WAMKULU
NDI WAMPHAMVU?
KUNAMA BASI.



MUNHTU
WOIPA. NDI
WODZALA NDI
UDANI.

TIKUTHYOLERA
CHITSEKO, TILOWA NDI
KUKUCHITA CHIPONGWE
CHOWAWA, MUNHTU
WOBWERA IWE.

INDE,
SITIKUFUNA ANA
AKO AAKAZI;
TIKUFUNA AMUNA
OKONGOLAWO.

AMBUYE MULUNGU
AKUCHITITSENI
KHUNGU.

ALI
KUTI?

NDANI
WAZIMITSA
MOTO? MDIMAWU
WABWERA
BWANJI?


MPHAMVU
IZI NDI ZA
MTUNDU
WANJI?

SINDIKUTHA KUWONA!
CHACHITIKA NCHIYANI?

UYENERA KUCHOKA MUMZINDA
MUNO MAWA MMAWA. UCHENJEZE
OYENERA KUWACHENJEZA. MULUNGU
NDI WOYERA NDIPO SADZALEKERERA
TCHIMO ILI.



MAWA MULUNGU
ADZAGWETSA MOTO
KUCHOKERA KUMWAMBA
PAMALO PANO. ALIYENSE
MU SODOMU NDI
GOMORA ADZAFU.



FULUMIRANI
MOTO WAKHALA
PANG'ONO KUGWA;
PALIBE AMENE
APULUMUKE.

MULINGU AKUTI
MUSACHELIKE M'MBLIYO
PAMENE MZINDAWO
LUKUYAKA.




**OSAYANG'AN
A M'MBLIYO**

EEEYI!



**OOO! ABAMBO,
AMAI SANAMVERE
MULLINGU. ASANDUKA
MCHERE.**

**OSAYANG'ANA
ZIMENEZO! MASO
PATSOGOLO!**




KAPENA AKAZI OKHAOKHA
AMAGONANA. MACHIMO
ACHIWEREWERE OCHITA
ANA OKHAOKHA NDI
ONYANSANSO KOPOSA.
MULUNGU ANALONJEZA KUTI
SADZAWONONGANSO DZIKO
LAPANSI NDI MADZI. KOMA

CHILICHONSE CHAMOYO
M'SO-DOMU NDI GOMORA
CHINAFAPA TSIKU
LIMENELO. MULUNGU NDI
WOLUNGAMA NDIPO AMADANA
NDI TCHIMO, MAKAMAKA
TCHIMO LACHIWEREWERE
MMENE AMLUNA OKHAOKHA

ZA MOTO SANANENEPO KANTHU. PAMENE
ADZAWONONGENSO ADZAWONONGA NDI MOTO.
CHILANGO CHA TCHIMO LILILONSE NDI IMFA: IMFA
YAKUTHUPI NDI IMFA YAMUYAYA M'NYANJA YA MOTO.
CHIFUKWA CHA CHISOMO CHA MULUNGU, LOTI
ANAPULUMUKA KU CHIWERUZO CHA MULUNGU. MKAZI
WAKE SANAKHULUPIRIRE ZIMENE MULUNGU
ANAWACHENJEZA KUTI ASACHEUKA M'MBUYO.

NTHAWI ZONSE
CHILANGO CHA TCHIMO
LA MTUNDU ULIWONSE
NDI IMFA BASI.





NDAKONDWERA KUTI
MULUNGU ADAKUKOMERA MTIMA.
LOTI, UKANAFU MU MZINDA UMENE
UJA. MULUNGU AMADANA NDI
TCHIMO NDI KUIPA KULIKONSE.
UZIDZIPATULA KWA
ANTHU OTERE.


TINALI NDI
CHISONI TITAMVA ZA
MKAZI WAKO. MUCHITA
CHIYANI TSOPANO?

TIONA MMENE
TICHITIRE. MOYO
WATHU SUDZAKHALA
MONGA KALE.

LOTI NDI ANA AKE AAKAZI
ANACHOKA NDIPO
MULUNGU ANAPITIRIRA
KUDALITSA ABRAHAMU.

GENESIS 19:24-26; LEVITIKO 18:22;
AROMA 3:23-32, 6:23; 1 AKORINTO
6:9-11; CHIVUMBULUTSO 21:8


MULUNGU ANALONJEZA
KUTI SARA ADZAKHALA
NDI MWANA. ABRAHAMU
NDI SARA ANAYAMBA
KUWONA ZIZINDIKIRO
ZA MALONJEZOWO.



ABRAHAMU,
CHIKUKUCHITIKIRA
NCHIYANI? KWA ZAKA
ZAMBIRI TSOPANO
SUNANDIWONEPO...
CHOTERE.



**CHINALI CHOZIZWITSA NDITHU!
PAKUTHA PA MIYEZI ITATU,
SARA ANABEREKA MWANA!**




MONGA MOMWE MULUNGU
ANANENERA TIDZAMUTCHA DZINA
LAKE ISAKE (KUTANTHAUZA
KUSEKA). ADZAKHALA TATE WA
FUKO LALIKULU.

INDE, PAMENE
MULUNGU ANANDIUZA
KUTI NDIDZAKHALA NDI
MWANA NDIDAASEKA.
NDANI AKANAKHULUPIRIRA
KUTI MU UKALAMBA
WANGAWU NKUYAMWITSA
MWANA WANGAWANGA?

MULUNGU
ANASUNGA LONJEZO
LAKE. AMATERO
NTHAWI ZONSE.

ISIMAELE, MWANA WA ABRAHAMU
AMENE HAGARA ANABEREKA,
ANALI NDI ZAKA 14 PA NTHAWI
IMENEYI, NDIPO ANKAMUDA
MWANA WAKHANDAYO.



KAMWANA KOPUSA
KAKUNDINYOZA.
SINDIDZALOLA KUTI
MUIGUPTO AKHALE
NYUMBA IMODZI NDI
ISAKE WANGA.

PIRIKITSA MKAZI
WANTCHITOYU NDI MWANA
WAKE YEMWE. SADZALANDIRA
CHOLWA CHILICHONSE NDI
ISAKE, MWANA WA
LONJEZO.



MULLINGU ANAYANKHULA NDI
ABRAHAMU NATI, "SARA AKUNENA
ZOONA. UCHOTSE HAGARA NDI
ISIMAELE. ISIMAELE SADZALANDIRA
CHOLWA PAMODZI NDI ISAKE. KOMA
USAKHUMUDWE NDI ZIMENEZI; INE
NDIDZAWASAMALIRA. NDIPO CHIFUKWA
CHAKUTI ISIMAELE NDI MWANA
WAKO, NDIDZACHITITSA KUTI MTUNDU
WAKULU UTULUKE MWA IYEYO.
KOMA MPULUMUTSI WOLONJEZEDWA,
AMENE ADZAGONJETSE SATANA
NDI TCHIMO, ADZACHOKERA MWA
ISAKE, OSATI MWA ISIMAELE."




ISIMAELE ANAKULA
NAKHALA TATE WA AARABU,
NDIPO ISAKE ANAKULA
NAKHALA MTSOGOLERI
WA AYUDA. AARABU NDI
AYUDA NDI ABALE
NDITHU (CHIFUKWA CHA
KHOLO LAO ABRAHAMU).

GENESIS 21:1-3, 9-14 *DZINA LOTI
ISAKE LIMATANTHAUZA KUTI
KUSEKA



NDIWE MWANA WA
CHOZIZWITSA. KODI
UDZAPULUMUTSA DZIKO
LAPANSI KU UCHIMO?

ABRAHAMU
ANKAMUKONDA
KWAMBIRI ISAKE.



ATATE, NCHIFUKWA
CHIYANI MUKUPHA
ANAANKHOSA
OKONGOLAWA NDI
KUWAOTCHA PA MILU
YA MIYALA?

MULUNGU WAKUMWAMBA
NDI WOYERA KWAMBIRI,
WOSAYENERA KUYANJANA
NDI MUNTHU WOCHIMWA
NGATI INE. MUNTHU
WOYAMBA, ADAMU
SANAMVERE MULUNGU NDIPO
KUCHOKERA PAMENEPO
MTUNDU WA ANTHU NDI
WOCHIMWA.

NDIKAPHA MWANAWANKHOSA
NDIKUMPEREKA KWA MULUNGU,
NDIMATSIKIZA ZA KUCHIMWA
KWANGA NDIPO MWANAWANKHOSA
WOSALAKWAYO AMAFA M'MALO
MWANGA.


MULUNGU
ADAAMUZA ADAMU KUTI
AKADZACHIMWA ADZABA,
KOMA ADAMU ATACHIMWA,
MULUNGU ADAPHA NYAMA
NAGWIRITSA NTCHITO
ZIKOPA ZAKE KUVEKERA
MANYAZI A ADAMU
NDI HAVA.



ISAKE ANAKULA NDIPO ANAPHUNZIRA KUDALIRA
MULUNGU WA ATATE AKE. ABRAHAMU
ANKAMUKONDA KWAMBIRI NDIPO ANKAPITA NAYE
LIMODZI KOKAPEMBEDZA NDI KOKAPEREKA
NSEMBE. MWANAWANKHOSA ANKAPHEDWA NDIPO
ANKAMUIKA PA GUWA LA NSEMBE KUTI AMUOTCHE.

**ABRAHAMU, NDIFUNA KUTI
LITENGE MWANA WAKO YEKHAYO
ISAKE, AMENE UMANKONDA,
NDI KUKAMPEREKA KWA INE
NGATI NSEMBE YOPSEREZA.**





AMBUYE, MUKUNDIUZIRANJI
KUCHITA CHINTHU CHOTERE? ZIKUKHALA
NGATI KUTI SINDINU AMENMUKUYANKHULA
CHONCHI. AKUNJA NDIWO AMAPERNSEMBE
ANA AO! MUNATI KUPYOLERA MWA MWANA
WANGA ISAKE MUDZAPANGA MTUNDU
WAIKULU. NDIKAMUPHA LONJEZO LANU
SILIDZAKWANIRITSIDWA.



...KOMA NDINU
MULUNGU. NGAKHALE
SINDIKUZINDIKIRA ZA
ZIMENE MWANENA,
NDIDZAKUMVERANI.


GENESIS 22:2; AROMA 5:12



YENDANI BWINO,
NDIZIKUPEMPHER
ERANI.


NDI ULENDU WA
MASIKU ATATU, NDIYE
KUTI KUPITA NDI
KUBWERA KUTITENGERA
SABATA NDITHU.

PATAPITA MASIKU ATATU.




ATATE,
PHIRI LAKE NDI
ILO. TIKAFIKA
KUMENKO USIKU
KUSANADE.

INDE, TIKUPITA
KUKAPEMBEDZA
NDIPO
TIBWERERANSO
KUMUDZI.




ATATE, TABWERA
NDI NKHUNI, NDIPO
MWAMANGA GUWA,
KOMA NANGA NSEMBE
YAKE ILI KUTI?

ISAKE, UKUMBUKIRA
KUTI NDIDAKUUZA ZOTI
MULUNGU ADAYANKHULA NDI INE
NACHITITSA KUTI INE NDI AMAI
AKO TIKHALE NDI MWANA MU
UKALAMBA WATHU? CHABWINO,
ADANDIYANKHULANSOTU.



PANOPA AKUTI
NDIKUPEREKE
IWEYO MONGA
NSEMBE.

INEYO?
ATATE,
KOMA NDI
ZONA?



KODI MULUNGU SADAKUZENI
KUTI INE NDIDZAKHALA
MLOWACHUMA WANU,
MTSOGOLERI WA
MTUNDU WAUKULU, KUTI ANA
ANGA ADZAKHALA AMBIRI
MONGA NYENYEZI
ZAKUMWAMBA? NDIKAFI LERO,
NANGA ZA LONJEZO
LA MULUNGULO?

NDAPHUNZIRA KUTI
ZIMENE MULUNGU AMALONJEZA
AMAZICHITADI. NGATI AKUTI
UDZAKHALA TATE WA FUKO
LALIKULU, UDZAKHALADI,
NGAKHALE UTAFI LERO.



KOMA
ZINGATHEKE
BWANJI
NDITAFU?

SINDIKUDZIWA,
POKHAPOKHA
ATAKUTSA KWA
AKUFA.

ATATE, TIYENERA
KUMVERA MULUNGU NGAKHALE
ZITAVUTA BWANJI.

GENESIS 22:3-9

NGAKHALE ABRAHAMU
ANKADZIWA KUTI AKUMVERA
MULUNGU, NKUTHEKA KUTI
ZIMENEZI ZIDAMUDE TSA
NKHAWA NDIPO MANJA AKE
ANKANJENJEMERA PAMENE
ANKATSATIRA DONGOSOLO
LOPEREKERA NSEMBE
YOPSEREZA.



ADAMANGA MANJA NDI MIYENDO YA MWANA
WAKE NDIPO ANAMLIKA PA GUWA LA NSEMBE.
CHOTSATIRA CHINALI CHAKUTI ATENGE MPENI
NDI KUMCHEKA PA KHOSI.

NDI PEMPHERO LA
CHIKHULLUPIIRO,
ABRAHAMU ANANYAMULA
MPENI. PAMENE AMATI
AMCHEKE PA KHOSI,
MWADZIDZIDZI ANAMVA
MAU KUCHOKERA
KUMWAMBA.



A comic book panel featuring a close-up of a hand holding a wooden staff. The hand is rendered in shades of brown and tan, with detailed line work showing the grip. The staff is light-colored wood. In the background, the face of a man with a long, white beard and a turban is visible, looking towards the viewer with a serious expression. The background is filled with diagonal hatching lines. A yellow speech bubble with a jagged edge is positioned in the upper right quadrant.

**ABRAHAMU!
ABRAHAMU!
USAMPWETEKE
MWANAYO.**



**TSOPANO
NDIKUDZIWA KUTI
UMANDIKHULLUPIRIRA,
POPEZA UNALI WOKONZEKA
KUNDIMVERA, MPAKA
KUPEREKA MWANA WAKO
MMODZI YEKHAYO.**

PAMENE ABRAHAMU ANAYANG'ANA
KUMWAMBA, ANAWONA NKHOSA
YAMPHONGO YOGWIDWA NYANGA
ZAKE M'ZIYANGOYANGO.



ATATE,
ONANI
MULUNGU
WATUMIZA
NKHOSA
YAMPHONGO
M'MALO
MWANGA!

**ABRAHAMU, POPEZA
WACHITA ICHI,
OSANDIMANA MWANA
WAKO MMODZI YEKHAYO,
NDIDZAKUDALITSA NDIPO
NDIDZACHULUKITSA ANA
AKO, ADZAKHALA NGATI
NYENYEZI ZAKUMWAMBA
NDIPO ANA AKO
ADZATENGA DZIKO LINO
NADZAWONONGA ADANI
AKO. KOMANSO,
KUPYOLERA MWA MWANA
WAKO AMENE SANABADWE
PALI PANO, MITUNDU
YONSE YA DZIKO
LAPANSI IDZADALITSIKA.**

GENESIS 22:9-18; AHEBRI 11:17-19



**ATATE, NDI
MULLINGU WABWINO
MONGA MUJA
MUNANENERA!**

ABRAHAMU ANALI NDI ANA AWIRI, ISIMAELE NDI ISAKE. ISAKE ANALI MWANA WOSANKHIDWA NDI MULUNGU KUTI AKWANIRITSE LONJEZO LAKE KWA ABRAHAMU. ISAKE ANALI NDI MWANA WOTCHEDWA YAKOBO, AMENE DZINA LAKE LINASINTHIDWA KUKHALA ISRAELE. YAKOBO ANALI NDI ANA AAMUNA 12, AMENE PA NTHAWI INA, ANAPITA NDI MABANJA AO KU IGUPTO KUMENE PAMBUYO PAKE ANAKHALA AKAPOLO (1875 B.C.).



GENESIS 21:5, 13, 24:67, 25:12-18, 21-26, 29:23-30

ANA AAMUNA 12 A
YAKOBO ANASANDUKA
MAFUKO 12 A ISRAELE.

ISIMAELE ANALI
NDI ANA 12 NDIPO
ANASANDUKA
MTUNDU WA AARABU.

ISIMAELE

ABRAHAMU

ISAKE
(1896 B.C.)

YAKOBO
(1836 B.C.)





<https://goodandevilbook.com/>